WEEKEND NATION
LOWERUKA, 22 APRIL 2023



Mitengo ya tsanya munkhalango ya Mwabvi

# Adaundaulira kuti asamalire mitengo yatsanya

WOLEMBA:
MARTIN GELA

Akuluakulu a nkhalango ya Mwabvi m'boma la Nsanje ati pakufunika kugwirana manja ndi kutetezera mitengo ya tsanya yomwe ili pa chiopsezo chachikulu choti ikhoza kutha ndi anthu omwe azungulira nkhalangoyi.

Mkulu woyang'anira khalangoyi a Brave Madise anati amakhumudwa kuti anthu ambiri akumaononga mitengo yambiri yatsanya potetha makala ndi kugulitsa pamtengo wotchipa kwambiri.

A Madise anati: "Mtengo umodzi watsanya unapatsidwa mtengo wa K8 miliyoni ngati utakoloredwa pomwe ambiri amabwera kudzadula mitengoyi ndi kutentha makala omwe ambiri amakhala akubwekera kuti ndi abwino kwambiri ndipo amayaka bwino. Tili ndi mantha kuti tsiku lina tidzapezeka opanda mitengoyi yomwe yapanga mbali yaikulu ya nkhalango ya Mwabvi."



A Madise: Mitengo ya tsanya siyololedwa kuti anthyu ayidule

CHITHUNZI: MARTIN GELA

Iwo adayamika bungwe la Shire Valley Transformation Programme (SVTP) ndi thandizo lochokera ku Global Environment Facility (GEF) lathandizira kuti mafumu ndi anthu awo omwe azungulira nkhalangoyi kuti akhazikitse mabungwe wotchedwa Natural Resources Committees (NRC) omwe akumathana komanso kugwira anthu woba mitengo ngati ya tsanya.

Malingana ndi a Madise mitengo ya tsanyayi siyiloledwa ndi boma kuti idulidwe ndi kugwiritsa ntchito ina iliyonse ndipo boma kudzera ku nthambi yoona za nkhalango ndi nyama za kutchire likuonetsa kuti mitengoyi ndi yotetezedwa.

Mwachitsanzo, iwo adati m'zaka zingapo zapitazo anakwanitsa kumanga nzika zina za m'dziko la China akuba mitengoyi koma bwalo la Nsanje First Grade Magistrate linapereka chilango cholozeka, thalakitala lomwe amagwiritsa ntchito poba katunduyu analipereka kuboma la Malawi pomwe mitengoyo analamula kuti ayiotche zomwe zinachitikadi popeza wina aliyense yemwe anagwiritsa ntchito mitengoyi anakapalamula mlandu wopezeka ndi katundu wotetezedwa ndi boma.

A Gulupu a Kambelengende a kwa Tengani anati amathandizira kuteteza mitengoyi chifukwa ikutetezera mitsinje ya Mwabvi ndi Thangadzi yomwe ambiri kudera la Misamvu amagwiritsa ntchito.

Iwo adati: "Magogo anthu a Tengani ndi a Mbenje anatiuza kuti nkhalango ya Mwabvi ndi mitengo yatsanya ndi chuma cha boma. Chifukwa kumabwera alendo omwe amadzaona malowa ndiye ngati tidula kapena kuononga tsanya ndiye kuti Mwabvi adzakhala dzina lokha komanso ana athu womwe tikuberekawa sadzamudziwa tsanya, pambali poti amalembedwa ntchito zosiyanasiyana."

Iwo adati kuchuluka kwa mitengoyi mbali mwa mitsinje iwiri ikuluikulu ya Mwabvi ndi Thangadzi kumapangitsa kuti anthu omwe tazungulira nkhalangoyi tisaone tsoka la madzi wosefukira, komanso nyama za kutchire ngati njati, njoka ndi zina zizipeza malo okhala abwino.

A Gulupu Chinthumba anathokoza a Mwabvi ndi SVTP powapatsa mbuzi zomwe akuweta zomwe zachititsa anthu m'deralo kuti achilimike paulimi ndi kusiya kuononga za chilengdwe kuphatikizirapo mitengo ya tsanya.

Pofuna kuonetsetsa kuti za chilengedwe zikusamalika mmalo onse omwe a SVTP akugwirako ntchito kudzera ku thumba la GEF anaika $5.6 miliyoni kuti zitetezere nkhalango za Mwabvi, Matandwe, Elephant Marsh, Thyolo Escarpment, Lengwe, Majete komanso Thambani. ■

## BWALO LA ULIMI



WOLEMBA: ANDREW SAUKANI

# Trade yadza ndi mphamvu

M'zaka zingapo zimene ndakhala ndikugwira ntchito yaza ulimi zimakhala zomvetsa chisoni kuti mapolojekiti a ndalama zankhani nkhani amayamba ndi malonjezo a bwino kuti apindulira alimi motere, adzapatsidwa maphunziro otere, adzalandira zipangizo izi ndi izo, adzaguliridwa zinthu izi ndi zina zoterozo.

Malonjezo amakhala a bwino ndithu kuti zitati zakwaniritsidwadi moona mtima zingathe kuthandiza kutukula miyoyo ya anthu m'maderamu komanso chuma cha dziko lino.

Alimi amakhala ndi chiyembekezo chachikulu kuti zinthu ziyenda osadziwa kuti mapulojekiti ena amasanduka mgodi wa ogwira ntchitowo. Tazionapo anthu akumanga mahotela n'kumalepheranso kumaliza, kuyambitsa makampani a mabasi chonsecho munthu analibe kena kali konse zili ndalama zakuba kudzera m'mapulojekiti.

Ngakhale awo amayendetsa mapulojekiti amanamizana kuti mbuzi imadya pamene ayimangilira koma dzifunseni kuti kodi anthu a kumudzi ngakhale si a dera lanu akhale makwerero a ulemelero wanu pamene iwo palibe chimene chikuchitika posintha miyoyo kapena madera awo?

Kumeneku ndi kuba ndipo kudandaula kwa anthu a ku midzi likhale gwero la masautso pamene mukudya chuma chanucho. Ulemu upite kwa iwo amene amakwaniritsadi zonse zimene alonjeza alimi m'pulojekiti imene apatsidwa danga kuyendetsa ndipo tikhulupilira alimi sagwiritsidwa fuwa la moto.

Transforming Agriculture through Diversification and Entrepreneurship (Trade) ndi pulojekiti ya zaka 6 kuyambira 2019 mpaka 2026 imene ikulandira ndalama kuchokera ku mabungwe a Opec ndi Ifad komanso boma la Malawi n'choliga chotukuka ulimi wa mtedza, soya, mbatata ya kachewere, kuweta njuchi, ng'ombe za nyama ndi mkaka m'maboma 11 a dziko lino.

Izi zithandiza kusintha miyoyo ya alimi kuti azionjezera phindu pa zokolola zawo zisanafike kumsika. Alimi ang'onoang'ono akuyenera kuthandizidwa kulima zochuluka, kumazikonza mwapadera kotero azikazigulitsa pakamodzi nkumapeza phindu. Alimi adzapatsidwa mwayi wa ngongole kudzera m'thumba la Agricultural Commercialization and Innovation Fund (Acif) koma alimi zindikirani kuti iyi si mphatso koma ngongole imene ikuyenera kumadzabwezedwa.

Alimi aphunzitsidwe luso lofunika malingana ndi magawo amene akuchita. Alimi akuyenera kukhala ndi luso lokambirana ndi ogula kuti malonda azikatha kukhala opindulira onse. Alimi adziwe malamulo a malonda, kayendetsedwe kabwino ka makoperativu, kasamalidwe ndi kakonzedwe kapamwamba ka zokolola komanso kapezedwe ka misika.

Pulojekitiyi ikutsindika kuti amayi ndi achinyamata atenge nawo mbali. Padzakhala kumanga malo osungiramo zinthu ndi misewu yabwino kuti mayendedwe kukafikira ku misika ikhale yosavuta.

Nkhani ya kusintha kwa nyengo ndi kakonzedwe ka zakudya zathanzi pakati pa alimi zidzaunikiridwanso. Polimbikitsa kugwilira ntchito limodzi, ku khonsolo kumene kukuchitika pulojekiti, kunasankhidwa munthu ogwira ntchito m'boma kukhala mlumikizi pa zochitika zonse kumbali imene ikuyendetsa polojekitiyi ndi nthambi zaboma. ■

Mafunso: saukaniandrew@gmail.com